Chewa version

JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION

"Promoting Faith and Justice"
P.O.Box 37774
10101 Lusaka, Zambia

Tel: 260-1-290410 fax:260-1-290759
E-mail:jctr@jesuits.org.zm web: www.jctr.org,zm

01 February 2006.

Moni kuchokera ku JCTR!

Mtendere wa Khristu.

Ife ndife okondwera kwambiri pokutumizirani mitu ya uthenga wa lenti wa caka cino ca 2006. Tingakhalenso okondwa ngati mau ya ciphunziso ca cikatolika azayetsa kuthandiza pakagawidwe ka uthenga wanyengo ino ya lenti. Tizindikira kuti mitu imeneyi izayetsetsa kuthandiza anthu amene ali ndi cigawo cotumikira m'mpingo wathu powona zomwe zili kucitika.

Pozindikira mayankho omwe takhala tiri kulandira pa zaka zapitazi, tizindikira kuti mitu imeneyi ya uthenga itha kutithandiza muzimbumba, mu magulu a misonkhano ya acinyamata ndi atsikana, ndiponso m'magulu athu amapemphero.

Tsono, munyengo ino ya lenti, ceni-ceni comwe JCTR ipempha akhristu onse n'cakuti, tonse tikhale anthu ogwapo pa nkhani ya masankho omwe tizakhala nawo mutsogolomu. Pemphero lathu n'lakuti masankho amenewa akakhale a bata ndi mtendere. Ndipo zimenezi zingatheke ngati tonsefe tayamba kuwona ndimaso odekha omwe tizindikira kuti tingabvotere panthawi ija. Pakucita zimenezi, tifunikira kuzindikira za cikondi ca Mulungu comwe cinawonekera mumasautso, imfa, ndi kuuka kwa ambuye Yesu pasiku pa sabata.

Tipereka mathokozo kwa ansembe, Abambo Smart Chinyanwa, S.S aku Emmaus Spirtuality Centre potikonzera uthenga wa lenti wa caka cino ca 2006.

Ife kuno ku JCTR tikufunirani mafuno abwino a lenti ndiponso tingakondwe ngati mungatithandize potuma maganizo anu pa mitu iyi ya uthenga. Maganizo anu ndizomwe mwakhala muli kuwona zingathe kuthandiza kutukula tsogolo lathu!

Ngati mungafune mau a uthenga umenewu muma computara, mungatifikire pa jctr@jesuits.org.zm.

Zikomo!

Simson Mwale
Bboloka Bubala Nchimunya, S.J.

Chewa version

LAMULUNGU LOYAMBA LA LENTI – CAKA B 5TH MARCH, 2006

Mau Oyamba: **Genesis 9:8-15**
Mau Aciwiri: **1 Petro 3:18-22**
Uthenga Wabwino: **Mariko 1:12-15**

NTHAWI YAKWANA

Taganizirani munthu wodwala malungo apita ku cipatala. Akudandaula kuti wakhala ali kumwa mankhwala koma bvuto lake osacoka. Motero, adotolo aganiza kuti ntahwi yakwana kuti apime magazi ake kuti afune tidoyo ta malungo. Koma munthu uyu n'kukana cifukwa ali ndi cikhulupiriro cakuti magazi ndi cinthu codara kotero kuti ndikosayenera kupima magazi. Kodi mungaganize zotani za munthuyo? Anataya nthawi yabwino yopezera thandizo.

Lero ndi la Mulungu loyamba la Lenti, nyengo yokwanira ngati milungu isanu ndi masiku asanu. Ndi nthawi imene tifunika kugwapo mwakhama kupunguza, kupemphera ndi kuthandiza anzathu. Zonsezi ziperekedwa kwa ife ngati njira yotembenukira moona. Yesu mu uthenga walero akuti "nthawi yakwana!" Cifukwa umoyo wathu uli ndi nthawi yake yofunika kuti titembenuke ndi kukhulupirira uthenga wabwino. Tsono Lenti ndi nthawi yapadera yomwe Mpingo wathunthu uika mapemphero ake onse pamodzi kuti anthu atembenuke.

Pomwe tiyamba nyengo yopatulika ya Lenti, Yesu akutiitana kupita naye pa ulendo wa ku cipululu. Kuitanidwa uku kungakhale koopsa! Kwa inu amene munapitako kumbari ya Kumwera {Western Province} kwa dziko lino, mudziwa kuti mu cipululu mulibe zifunikira pa umoyo wathu. Mwa zoonadi, cipululu cifuna wodzimana, wokhulupirira ena ndiponso wodzicepetsa. Tsono n'cifukwa ninji kuti munthu afune m'khalidwe wa m'cipululu.? Cifukwa munthu akhale wodzibvutitsa, wokhulupirira thandizo la ena, ndi wodzicepetsa?

Yesu ayankha mafunso otere mu uhtenga wabwino: "Nthawi yakwana, Ufumu wa Mulungu uli pafupi kukhazikitsidwa. Lapani ndi kukhulupirira Uthenga wabwino." Kwa iwo amene ali pa malonda, mwa citsanzo ogulitsa pa msika, anena kuti kapimidwe ka nthawi ndiye cinthu copambana. Anthu ngakhale kuti ali ndi ndalama zambiri akulephera kupeza bwino mu malonda ao kamba kosadziwa nthawi. Nzonadi nthawi ikanakhalapo, koma nthawi ndi yaciani? Yesu akuti, "Ufumu wa Mulungu uli pafupi. Lapani ndi kukhulupirira Uthenga wabwino."

Poyambirira, Lenti ndi nthawi imene tikonzekera kukondwerera cikondi ca Mulungu comwe cimaoneka mu misteri ya kuzunzidwa, kufa ndi uka kwa Yesu Khristu. Tsono tikonzekera bwanji cikondwerero ici? "Lapani ndi kukhulupirira Uthenga wabwino" akutero Yesu. Iye akutiitana kuti tisinthe makhalidwe athu ndi kudziphatikiza ndi Uthengo wabwino umene ndi Yesu yemwe. Monga umanenera mwambi wina wa Cibemba "Ukwali insoke, takwafwile muntu", kutanthauza kuti ziziwitso zimatetedza imfa. Tsono ndi koyenera kumva mau olangiza. Nthawi yakwana yoti tifufuze makhalidwe athu ndi anzathu ndi kugapo kudzetsa cilungamo ndi mtendere, cikondi ndi kulemekezana.

Kwa ife anthu am'dziko la Zambia, nthawi yafikanso, yomwe tizasankhula atsogoleri athu. Caka cino ca 2006 tizakhala ndi masankho amtsogoleri wa dziko {Presidential elections}, aphungu anyumaba ya malamulo {Parliamentary elections} komanso masankho aatsogoleri aboma am'madera osiyana-siyana {Local Government elections}.

La Mulungu loyamba la Lenti, Yesu akutikumbutsa inu ndi ine kuti caka cino ndi zones zomwe zizacitika ndi mphatso ya Mulungu yomwe siifunika kuonongedwa. Tizindikira tonsefe kuti pa nthawi zoterezi pamakhalanso zinyengo zambiri.

JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION
"Promoting Faith and Justice"
P.O. Box 37774 10101 Lusaka, Zambia
E mail: jctr@jesuits.org.zm

Nthawi yatifikira yoti tisankhule atsogoleri omwe azadzipereka kwathunthu ndipo mwa khama pa utsogoleri wao m'dziko lino. Koma utsogoleri umenewu uzatha kusankhulidwa ngati tonse tinalembetsa masankho, tidzatsira sankho {vote} lathu kapena tizagwapo pakusankhula atsogoleri athu ngati nthawi yace yafika. Utsogoleri umeneu uzatheka pokhapo ngati ife tazipereka kwathunthu ndipo mwa khama mu zinchito ndi maudindo athu osankhula atsogoleri. Nchifukwa cake kuchokera mu caka ca 1978, aziepiskopi achikatolika mukalata yawo, masankho asanacitike m'caka cimeneci, anati, "Tikupempha anthu onse kuti agwiritse nchito kofikapo ufulu wao wosankhula atsogoleri chifukwa iyi ndi nchito ya mkhristu aliyense." Pakutero, akhristu alugwapo pakudzetsa ulamuliro wabwino wotumikira ndi kuthandiza anthu onse.

Nthawi zina ife akhristu tingathe kudzuzula atsogoleri mopitilira malire chifukwa mwina tiganiza kuti pakutero, tigwira nchito yakuitanidwa kwathu. Koma ngati nthawi yoti tisankhule atsogoleri athu yafika, timalephera kutengako mbari mumasankho chifukwa sitimvetsa kuti iyinso ndi nchito yathu akhristu. Nafenso timacita ngati munthu uja wodwara koma safuna kupimidwa. Nthawi zones tifunika kupedza gwero la bvuto lathu. Tiyeni tisankhule atsogoleri omwe adzatsogolera dziko lathu kuti tipeze chitukuko, chilungamo ndi mtendere wa azimai, azibambo ndi ana. Ndi pemphero lathu kuti tizatsenza udindo wathu wosankhula atsogoleri moyenera, mwakhama ndipo mofikapo, "kukumbukira kuti nthawi yafika."

Kusinkha-sinkha pa mafunso ndi kugawana muzimbumba kapena mabungwe.

- Kodi ndi zinthu zotani zomwe ndizacita pa nthawi yino ya Lenti ? Mwacitsanzo, Kupungidza {Fasting}, Mapemphero{Prayer}, ndi Kuthandiza osowekera {Almsgiving}.
- Kodi ndine wokonzeka ndi wozipereka kutengako mbari pa masankho omwe akubwera? Chifukwa? Ngati sindine wokonzeka, chifukwa?
- Kodi ndi mphatso kapena zizindikiro zotani zabwino zomwe ndifunika kuyang'anapo kapena kudziona mwa anthu onse amene afuna kuimilira pa masankho kuti asankhidwe atsogoleri athu.?

Tsewero {sketch}

Sankhani mwamuna wodwala amene azapita ku cipatala pamodzi ndi anzake kapena mkazi wace. Atafika kucipatala, mwamuna uyu azadandaula za mphepo, kupweteka kwa mutu ndi kupweteka kwa thupi lonse. Adotolo azapempha kuti munthu uyu apimidwe chifukwa atha kukhala ndi malungo{Malaria}. Koma munthuyu, adzakana kuti apimidwe ndikucoka kucipatalako.

Mapemphero

- Ambuye, tithandizeni kuti tithe kuzindikira ndi kudziwa za kusowekera kwa anzathu. ***Ambuye Mutimvere.***
- Ambuye, tipatseni mphamvu ya mzimu woyera kuti tithe kudzipereka pa nchito yodzetsa chilungamo, mtendere ndi chikondi pakati pathu. ***Ambuye Mutimvere.***
- Ambuye, pomene tilikuyamba nthawi yino ya Lenti, tipemphera kuti tibvomere kuitana kwanu kuti tilape ndi kubvomera uthenga wabwino. ***Ambuye Mutimvere.***

JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION
"Promoting Faith and Justice"
P.O. Box 37774 10101 Lusaka, Zambia
E mail: jctr@jesuits.org.zm

LAMULUNGU LA CHIWIRI MU LENTI CHAKA B 12th March, 2006

Mau oyamba: **Genesis 22:1-2. 9-13. 15-18.**
Mau achiwiri: **Aroma 8:31-34**
Mthenga Wabwino: **Marko 9:2-10**

"NDIKWABWINO KUTI IFE TIKHALE PANO"

Mu uthenga Wabwino wa lero, atatu mwa Ophunzira a Yesu, Petro, Yohane ndi Yakobe adali odabwa pa kuona kuti maonekedwe a Yesu adasinthika iwo akuona. Ndipo Petro m'malo mwa anzake anati: *"Aphunzitsi ndikwabwino kuti ife tikhale pano. Tiloleni kuti timange misasa itatu."* Pakunena zimenezi, Petro akufuna kutanthauza kuti umwai umene anali nao woona kusandulika ndi kuwala kwa Yesu Khristu kupitirize. Anali kufuna kuti apitirize kuona ulemerero umenewu mpaka muyaya.

Kodi zimenezi sizimaoneka mu umoyo wathu? Ndi angati mwa ife amene anakakonda kuti cimwemwe cimene anali naco pa caka ca ukwati wao, kapena caka ca malumbiro ao ya umai, kapena caka ca unsembe wao cipitirize? Ncifukwa cake ena amati: kuipa kwa zinthu zabwino ndi kwakuti zimatha nthawi ikakwanira.
Koma Yesu akudziwa bwino lomwe kuti ulemerero wa kusandulika kwake udzafika pa cimake cheni-cheni ngati iye adzatsatira njira ya masautso ya ku Golgotha. Ngakhale pamene anaona ulemerero wa pa Phiri la Tabor, Yesu sanataye colinga ca utumiki wake, copulumutse anthu onse. Zimenezi zinamthandiza kutsatira colinga cake.

Mu cowerenga coyamba tamva za Abraham, kholo lathu mu cikhulupriro amene anabvomera kusiya dziko lake ndi kutsata kuitana kwa Mulungu. Anabvomera kucita cifuniro ca Mulungu mwa cikhulupiriro. Monga tidziwa bwino lomwe kuti Abraham ndi mkazi wake Sara anali okalamba pamene adaona mwana wao woyamba, Isaki. Motero lonjezo lomwe Mulungu anapangana ndi Abraham kuti adzakhala ndi pfuko lalikulu lidzakwanilitsidwa. Ili linali lonjezo lokoma kwambiri kotero kuti Abraham ndi mkazi wake akananena kuti: *"Ndikwabwino kuti zikhale tero."* Koma Mulungu anamchotsa pa mtendere umene anali nao cifukwa cakuti iye yemwe anabvomera kuitana kwa Mulungu. N'cifukwa cake lero tikumchula kuti ndi atate wathu mu cikhulupiriro.

Umoyo wathu wa uzimu uli ngati ulendo. Mkhristu aliyense woona ali pa ulendo. Nthawi zonse amayesesa kuzindikira mwa mphamvu ya mzimu woyera nchito zimene Mulungu akufuna kuti agwire mu umoyo wake. Mwa njira ya padera, Lenti ndi nyengo m'mene ife tipemphedwa kuyenda ndi Khristu, kusiya zinthu zotikondweretsa ndikucita zimene Mulungu afuna.

Uthenga umenewu ndiwofunikira kwambiri kwa ife mu dziko lathu lino la Zambia, maka-maka pa nthawi ino pamene tikuyandikira masankho. Ena mwa atsogoleri athu, omwe akhala paulamuliro kwa zaka zisanu, akunena ngati petro kuti: *"Ndikwabwino kuti tikhalebe paulamuliro."* Nkotheka kuti ena mwa atsogoleri athu azolowera kukhala pa ulamuliro kotero kuti sazindikira kuti angachoke ndi kukhala amodzi mwa anthu wamba. M'khalidwe woterewu ungapangitse atsogoleri athu kukhala ndi nkhawa ndi kucita ciliconse cotheka kuti apitirizebe kukhala pa ulamuliro. Kodi sicacidziwikire kuti munthu wankhawa angacite ciliconse ngakhale coseyenera?

Kodi atsogoleri athu a zandale, cifukwa cokondi dziko lathu la Zambia, sangadzipereke monga Abraham kholo lathu mu cikhulupiriro, kuti asiye zowakondweretsa ndi kutumikira athu anzao? Nanga ife amene tiri mu zipani zandale zosiyana-siyana, kodi kukhala mu cipani ca ndale ndi kofunikira kopambana kukhala nzika ya Zambia? Mwambi wina umanena kuti: "*Sunga khosi mkanda woyera udzafika."* Ngati mwapatsidwa danga losankha pakati pa khosi ndi mkanda, musankhe khosi cifukwa

JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION
"Promoting Faith and Justice"
P.O. Box 37774 10101 Lusaka, Zambia
E mail: jctr@jesuits.org.zm

mukanda mungathe kupeza wina. Cimodzi-modzi, ngati tifuna kusankha pakati pa cipani ca ndale ndi dziko lathu la Zambia, tiyeni tisankhe dziko lathu. Ngati tifuna kusankha pakati pa mtsogoleri ndi dziko tiyeni tsankhe dziko lathu.

Tiyeni tipemphere kuti pamene ife tonse tikukonzekera kukacita masankho, tikhale okonzeka kutaya mkanda kuti tisunge khosi limene liri dziko lathu la Zambia. Tipemphe Mzimu Woyera atsekule makhutu athu kuti timve kuitana kwa Ambuye, kuti tisiye zinthu zotikondweretsa, n'colinga ca kuti tiyende nawo Ambuye ku Phiri la masautso kotero kuti tikakondwere nawo mu ulemerero wa kuuka kwao. Pemphero lathu likhale lakuti: *"Ndikwabwino kuti tikhale pano, koma Ambuye mutipatse cikhulupiriro cozama pa ulendo wathu."*

Mafunso otithandiza kusinkha-sinkha ndi kugawana mu mabungwe/zimbumba

- Ine ngati mtsogoleri wa bungwe/mbumba, Ward kapena Constituency, kodi ndine wokonzeka kutula udindo wanga kuti ena alamulileko?
- Cofunikira kwambiri ndiciti paizi: mwacisanzo ngati ndapatsidwa mpata wosankha pakati pa banja langa ndi zondikondweretsa cabe ine, kapena pakati pa cipani canga ca ndale ndi zokhuza dziko lathu la Zambia?
- Kodi ndimayesetsa kutumikira ena kapena ndimafuna kudzikondweretsa ndekha?

Sewero

Pakhale ma banja awiri: banja lina likhale lolemera, lokwaniritsa zonse: cakudya ndi kukwaniritsa kupereka ana ku sukulu. Banja lina likhale losauka: losowekera madzi aukhondo, cakudya ndi kulephera kupereka ana ku sukulu. Mwana wamn'gono wa ku banja lolemera auza makolo ake za mabvuto amene apezeka mu banja la osauka lija, koma makolo ake saikako nzeru ku zimenezi.

Mapemphero a akhristu

- Tipemphe Ambuye kuti atipatse mphamvu zotithandiza kuti tikhale okhulupiririka pa nchito yathu yodzetsa cipulumutso pa dziko la pansi. *Ambuye mutimvere.*
- Ambuye kusandulika kwanu kunadzetsa cimwemwe kwa Ophunzira anu, mutithandize nafenso kudzetsa cimwemwe ndi cisangalalo pakati pa anzathu. *Ambuye mutimvere.*
- Ambuye pamene tikuyenda nanu pa ulendo wanu wo pita ku Golgotha, mutithandize kubvomera kuitana kwanu ku cisangalalo ca ulemerero wa kuuka kwaku. *Ambuye mutimvere.*

JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION
"Promoting Faith and Justice"
P.O. Box 37774 10101 Lusaka, Zambia
E mail: jctr@jesuits.org.zm

Chewa version

LA MULUNGU LA CITATU MU LENTI B. 19th March, 2006

Mau oyamba: **Exodo 20:1-17**
Mau Aciwiri: **1Korinto 1: 22-25**
Uthenga wabwino: **Yohane 2: 13-25**

CANGU COMWE NDIMACITIRA NYUMBA YANU CIZANDIPHESA

Pakati pa Ayuda, Tempile inali nyumba yoyera. Sidangowapatsa cabe malo aciyembekedzo ndi operekera nsembe, komanso inali cizindikiro ca Mulingu pakati pao. Kwa muyuda aliyense, ngati Tempile ilipo, Mulungunso alipo. Nyumba imeneyi inali citsimikizo cakuti Mulungu sadalekelere anthu ake, ngakhale kuti anali anthu ocimwa ndi ofooka. Ncifukwa cake, Tempile inali cinthu cacikulu mu umoyo wa Ayuda. Ncifukwa cakenso, Yesu anakwiya kwambiri pomwe anapeza anthu akucita malonda m'tempile, m'malo mwa cipembedzo.

Monga tikuona mu mthenga wa bwino, wa tsiku la lero, macitidwe a Yesu Christu oyeretsa Tempile pakupilikitsa anthu omwe anali ku gulitsa ndi kugula, asonyeza uneneri. Yesu anapya mtima pakuona kuti nyumba yokoma-koma inali kuwonongedwa. Pakutero, anacita cinthu coopyeza umoyo wake. Anatulusa onse omwe anali kucita malonda mu Tempilemo. Ici cidakwiitsa a Yuda ndipo anafuna-funa njira yoti ampheremo. Nanga kodi cinapasa Yesu mphamvu zocita zimenezi mopanda mantha nciani?

"Cangu comwe ndili naco ca nyumba yanu cizandiphesa". Awa ndi mau a mucipangano ca kale omwe adaza mumaganizo ya ophunzira a Yesu, poona mcitidwe wa Yesu. Siuyu munthu okonda coona, cilungamo, mkhalidwe wabwino, kotero kuti ndi okonzeka kudzudzula atsogoleri a mpingo pa nthawi imeneyo; pofuna kupititsa patsogolo makhalidwe abwino. Siuyu munthu ali okonzeka kufera khalidwe yabwino. A Chewa amati: *"Walila mvula, walila matope*". Kutanthauza kuti cikhristu ndikumvomera zonse zosatira cikhristu, ngakhale imfa imene. Tikumbukire mau ya mkulu wina wocedwa Martin Luther King Junior, yemwe analalika za ufulu wa munthu onena kuti, *"Aliyense amene asanapeze cinthu comwe aliokonzekera kuferapo, ameneyu alibe umoyo"*. Kodi inu ndi ine tinapeza kale cinthu comwe tingafere?

Panthawi ya masankho caka cino muno mu Zambia, zinthu zambiri zizacitika. Mwacisanzo, onse amene afuna kuiimirira m'masankho amenewa ocokera mu zipani za ndale zosiyana-siyana, azabwera ndi malonjezo awo abwino a zinthu zomwe iwo afuna kucita. Iyi ndi nkhani yabwino komanso yoyenerera cifukwa tizakhala ndi mpata wakumva zomwe atsogoleri athu azatipasa pambuyo pa kuwasankha. Koma, poona zomwe zaticitikira kumbuyoku, tonse tiziwa kuti ena mwa atsogoleri amenewa, azayamba kunyozana ndi kukhazulirana mau pamene ali kucita makamupeni awo. Kutero ndikugwiritsa nchito cinthu cabwino monga kamupeni pofuna kukwaniritsa zokomera iwo wokha –pofuna kupambana mosayenera.

Tsiku la lero, Yesu akufuna anthu olungama omwe aliokonzeka kutumikira, opanda mantha, ozipereka, komanso ali okonzeka kudzudzula makhalidwe oipa mopanda mantha. Zinthuzi zingatithandize kusanda-sanda anthu omwe afuna kuimirira pa utsogoleri. Ndithudi izi zizakhala ngati mpimo othandiza kucotsapo atsogoleri omwe amakonda kunyoza. Mwa njira imeneyi tizayeresa Tempile yakacitidwe ka masankho ndi makamupeni. Nkoyenera ndithu kukumbuka mau a Luntha omwe ma Episkopi a cikatolika anafotokoza mu caka ca 1996 masankho asanacitike; "cifukwa cake tipempha achristu onse kuti aonetsetse kuti zipani za ndale zifotokoza pfundo zoyenera, mwacisanzo, kuthandiza amphawi umoyo wabwino wa anthu onse, nkhani za ulimi komanso nkhani za maziko a cuma pamene ali kucita kamupeni. Kwa iwo omwe acita kamUpeni, popanda pfundo zimenezi, anthu omwe angokonda kunyoza anzao amabweretsa ciwawa nthawi ya masankho, ndipo nkosayenera kuwasankha."

JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION
"Promoting Faith and Justice"
P.O. Box 37774 10101 Lusaka, Zambia
E mail: jctr@jesuits.org.zm

Moonjezeranso, malo ena omwe ndiwofunika kuyeresedwa mu caka cino ca masankho ndi nyumba ya malamulo. Tonsefe tidziwa bwino kufunika kweni-kweni kwa dzanja ili ya boma pokhazikitsa malamulo okomera anthu onse, komanso ulamulilo wabwino. Masankho ndi mpata wathu tonsefe kuti tipyere ndi kuyeresa nyumba imeneyi ngati nkoyenera. Funso yomwe tiyenera kuzifunsa ndi iyi; kodi atsogoleri omwe tidasankhula agwira bwanji nchito pa zaka zisanu zapitazi? Kodi adaimirira ndi kulakhulira zofuna ndi zokomera anthu omwe anawatuma ku nyumba ya malamulo? Kodi adatiyendera ku madera athu? Mafunso awa ali ngati mpimo kwa anthu omwe afuna kuimirira pa utsogoleri. Masankho ali ngati cikumbutso kwa onse amene afuna kugwira nchito mu boma ndi mdziko lathu kuti, azafunsidwa ndi ise anthu pa zocita zao ndi pfundo zomwe anamanga akadali mu boma, ngakhale ndi a Presidenti, phungu wa nyumba ya malamulo kapena kansala.

Pasaka yayandikira pangokhala cabe Milungu inai tiyeni tipitilize kupemphera kuti nyengo ino ya Lenti, ikhale mpata kwa ife tonse kuti tione zomwe zifunika kuyeretsedwa aliyense pa iye yekha komanso ngati dziko. Tiyeni tipemphere kuti cangu comwe cinaphetsa Yesu pa mtanda cizaze mitima yathu ndi kutithandiza kufuna-funa cilungamo, m'masankho a caka cino osasamala zobwera pa umoyo wathu. Ncifukwa cake mau awa akale athu, "*Cangu ca mu nyumba yanu cizandiphesa."*

Mafunso othandiza kusinkha-sinkha ndi kugawa mabungwe/ mbumba

- Kodi mu umoyo wanga muli cinthu cotani comwe ndili okonzeka kufera pokhala m'khristu?
- Kodi atsogoleri a dziko lathu mu zaka zisanu zapitazi atsogolera motani?
- Kodi ndimalemekeza ndi kupatsa ulemu malo a cipembedzo?

Sewero

Pakhale anthu awiri omwe aimirire omwe akufuna kukhala atsogoleri (mwacisanzo, atsogoleri a Church Council, a Kansala). Oyambirira agwiritsa nchito msonkhano wa kampeni kunyoza, ciphuphu, kutukwana ndi kudzudzula anthu ena omwe nawonso ali kuimirira pa mpando umodzi-modzi, koma osafotokoza pfundo zokhuza anthu. Wina agwiritsa nchito ya kampeni kufotokoza pfundo za citukuko mdera lake.

Mapemphero

- Ambuye tipempha kuti mutipatse mtima wofuna cilungamo ndi kusapondelezana m'masankho a caka cino popanda kuziganizira ife tokha. Ambuye mutimvere.
- Ambuye, tikuzipempherera ife tomwe kuti tione zoyenera kuyeresa mu umoyo wathu komanso mu dziko. Ambuye mutimvere.
- Ambuye, tikupempherera atsogoleri athu kuti agwiritse nchito mwa ulemu mpata wa kamupeni ukubwerawu kufotokoza pfundo zokhuza anthu onse. Ambuye mutimvere.

JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION
"Promoting Faith and Justice"
P.O. Box 37774 10101 Lusaka, Zambia
E mail: jctr@jesuits.org.zm

Chewa version

LA MULUNGU LA CINAI MU LENTI-CAKA B: 26 MARCH 2006

Cowelenga coyamba: **2 Mbiri 36: 14-16. 19-23**
Cowelenga ca Ciwiri: **Aefeso 2:4-10**
Mtenga wa Bwino: **Yohane 3:14-21**

KUWALA KWAZA MDZIKO LA PANSI

Ife tonse tidziwa bwino kukoma kwa nyale. Popanda nyale, sitingazindikire kukoma kwa zinthu zapadziko lapansi. Mwanjira ya padera, nyale imatithandiza kuzindikila cabwino ndi coipa. M'njira imeneyi, nyale imatithandiza kupanga maganizo olungama. Monga tamva mu uthenga wa bwino wa tsiku la lero pomwe Yesu Khristu alukambilana ndi Necodemo, Yesu Khristu afotokoza kuti iye ndi nyale. Yesu Khristu ndi nyale yomwe yaza pa dziko lapansi. Yesu Khristu alingati mudzi womangidwa pa mwamba pa phiri, monga mwambi unena kuti , "Mudzi ukakhala pa phiri subisika". Mwa cisoni, Yesu Khristu alutifotokozela kuti, "Anthu amakonda mdima koposa kuwala." Ngati nyale ndiyofunika kwambiri pa umoyo wathu, cifukwa nciyani anthu amakonda mdima koposa kuwala?

Bambo wa panyumba pena anaitana mwana wace wamwamuna wazaka zakubadwa zokwanila khumi ndi ziwiri kuti akambiraneko. Msonkhano wa awiriwa unali ndi mfundo imodzi, yakuti akambirane pazakagawidwe ka nchito za panyumba. "Mwana wanga," adatero bambo, "ukaona zakagwiridwe ka nchito pa nyumba pano, kodi suganiza kuti iwe ndi ine tiluwapondereza amako ndi azilongo ako kumbari ya kagawidwe ka nchito za pa nyumba?" Mwam'sanga-m'sanga ndiponso mwaukali mwana uja adayankha adati, "ndilikukuthokozani pondifunsa, atate, koma ndidziwa motsimikiza kuti tsitiluwapondeleza ndipang'ono pomwe. Ponva yankho ya mwanayo, bambo uja adapitiliza kulankhula adati, "cabwino! Ndibwino kuti tikumbutsane pazinchito zomwe zigwilika panyumba pano matsiku onse, ndipo tione momwe zimagwilikila ndi adzigwila. Nthawi zonse tikauka m'mawa, nyumba imakhala yopyeledwa, timalandila cakudya cam'mawa ndiponso mbale dzimatsukidwa. Ndani omwe amagwila nchito zimenezi?" Mwana uja adayankha kuti, "Amai ndi azilongo anga." "Ndiponso ukaweruka kusukulu umapeza cakudya cam'matsana cakonzedwa kale. Pambuyo pa cakudya cam'matsana mbale zimatsukidwanso ndiponso cikonzekero cacakudya cam'madzulo cimayamba. Madzi amatungidwa ndiponso nkhuni zimatemedwa. Cakudya cam'madzulo cikakonzeka timaitanidwa ku kudya ndipo pambuyo pake mbale zimatsukidwa. Kodi iwe mumaganizo ako, ndani amagwira nchito zimenezi?" " Amai ndi azilongo anga." Adatero m'nyamatayo. "Mwana wanga, ndilikukufunsanso, kodi tsuganiza kuti amai ndi azilongo ako tiluwapondereza pakagawidwe kanchito zapakhomo?" Mwana uja adati, "tsopano ndazindikila kuti tsitilikuwatsunga bwino, koma ndapapata, atate, musawauze!"

Iyi ndiyo bvuto ya kuwala kapenanso bvuto lomwe anthu amakhala nalo pa zakuwala. Amaopa kuti angataye zabwino zomwe amapata ali m'mdima. Iwo omwe amapata zabwino cifukwa ca umbuli wa anzao, amayetsetsa kuti makhalidwe oterewa apite patsogolo. Kubvomera Yesu Khristu kutanthauza kuti kukhala ndi mphabvu yoona umoyo wathu momwe ulilidi. Kubvomera Yesu Khritu ngati nyale m'umoyo wathu kutanthauzanso kuti kubvomera mphabvu yake yotifuna-funa yomwe ingatsinthe zikhulupiliro zathu zakale ndiponso makhalidwe yathu omwe alutayana ndi umoyo wacikhristu.

Pomwe tilukonzekera masankho mdziko lathu la Zambia,ife tonse, a khristu ndi nzika za dziko lino, tikhale ndi udindo wozindikira zomwe zilucitika mdziko lathu. Pogwiritsa nchito kuwala kwa Yesu khristu ndiponso ciphunzitso ca mpingo pa mkhalidwe wa anthu, tifunika kumvetsa bwino momwe boma ifunikira kugwila nchito. Pokhapo ndipo tingathe kudziwa kusankhula anthu abwino omwe angatsogolere dziko lino. Ife tonse tisakhale ngati anthu oonerera mpira, koma tikhale ngati anyamata a mpira kutanthauza kuti tisangokhala oonerera cabe pazandale, koma tigwepo nutengapo mbali. Caka cino tisankhule kuwala komwe kwaza mziko lino. Masankho asanafike caka cino,tizipeleke mwathunthu pakugawana m'manyumba mwathu ndi m'zimbumba zathu kuwala kwa

JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION
"Promoting Faith and Justice"
P.O. Box 37774 10101 Lusaka, Zambia
E mail: jctr@jesuits.org.zm

uthenga wabwino ndinso ciphunzitso ca Mpingo pazamakhalidwe- monga kalamulilidwe ka dziko kabwino, ndiponso za cilungamo. Nyumba za mphepo; za boma kapenanso za m'madela athu, ndimbali zofunikira kwambiri kudziwitsa nzika za dziko ino pa zomwe zilucitika ndinso pazomwe magulu osiyana-siana yandale mdziko lino alucita. Nthawi zina, pambuyo pomverera nyumba za mphepo ndi makanema a boma, munthu angakhale ndi cithunzi cakuti gulu la ndale yomwe ilulamulira ilupikitsana mwa iyo yokha. Koma onse amutola nkhani omwe agwila nchito m'nyumba za mphepo, ali ndi udindo woziwitsa anthu, pa nkhani zokhuza dziko, moona ndiponso mwacilungamo.

Mkalata ya ma Episkopi acikatolika a dziko lino (pastoral letter) mcaka ca 2001, iwo anaunikira kuti, "Tikupempha zigawo zonse zomwe zili ndi nchito younikira anthu kuti, zisunge monyadira udindo wao woziwitsa ndi kuphunzitsa nzika pa nkhani ya masankho, kuti aziikapo mitu ya nzeru pazocitika mdziko. Zimenezi zionetsa ukatswiri wao, ndipo aonetsetse kuti magulu onse yandale aimililidwa molingana ndiponso mopanda tsankho.Tikuyembekezanso kuti cigawo cimeneci, counikira anthu, cizipanga mfundo zokwima zomwe anthu angakambiranepo pounguza-unguza pa nkhani za ndale za dziko. Mwanjira yapadera, tilupempha zigawo zonse za boma zounikira anthu monga; nyumba za mphepo ndi kanema, kuti zipereke mpata wolingana ku magulu onse a ndale."

Pomwe nyengo ya Easter iluyandikira, m'masabata atatu alubwera, tipemphe kuti tonse tidzasankha kuyenda m'njira ya kuona osati muucimo wa umbuli ndi mantha. Tipemphe kuti kuwala kwa Yesu Khristu kuunikire umoyo wa a Khristu onse kotero kuti mdima omwe umaza cifukwa ca anthu omwe ali ndi mantha kutaya danga yomwe alinayo yopata zinthu mwa njira yosayenera, upambanidwe. Umeneu ndiwo uthenga wa Easter- kuwala kweni-kweni kwa m'mawa mwa sabata ya Easter kwapambana mdima wa cisanu coyera. Ndithudi, "kuwala kwadza pansi-pano"

Mafunso Othandidza Kusinkha-sinkha ndi Kugawana Mzimbumba.

- Kodi ndilutengapo mbali yotani pazamasankho omwe alubwera ndiponso pazakayendetsedwe ka boma?
- Kodi ndiliokonzeka kuimira pa coona, ngakhale zibvute zitani?
- Kodi ndili okonzeka kusankhula Yesu Khristu m'umoyo wanga ngati nyale yomwe yabwera mdziko lonse lapansi ndiponso ndionetse bwanji kwa anzanga kuwalako?

Tsewero

Konzani banja la anthu asanu. M'banja limeneli, mai ndi ana ake awiri, azikazi, agwira nchito zonse za panyumba. Tsiku lina bambo wapanyumbapo pamodzi ndi mwana wake wamwamuna akambirana pazotengapo mbali pa nchito za pa nyumba, monga kukonza cakudya, kusuka mbale ndi kupyela. Pambuyo pake, mwana uja wamwamuna azindikila kuti ncofunikira kutengapo mbali pa nchito zapanyumba zomwe nthawi zambiri zimakhalira acimai okha.

Mapemphero ya Akhritu

- Ambuye, tikupemphani kuti tonse tisankhe kuyenda m'kuwala kwa coona osati m'mdima wa umbuli ndi mantha. **Ambuye mutimvere.**
- Ambuye tikupemphani kuti kuwala kwa Yesu Khristu kuunike kosalekeza mu moyo wa a khristu onse. **Ambuye mutimvere**.
- Ambuye, dalitsani mabanja athu panyengo ino yamadalitso. **Ambuye mutimvere**.

JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION
"Promoting Faith and Justice"
P.O. Box 37774 10101 Lusaka, Zambia
E mail: jctr@jesuits.org.zm

LAMULUNGU LA CISANU MU LENTI – CAKA B: 02 APRIL 2006

COWERENGA COYAMBA: YEREMIYA 31: 31-34
COWERENGA CACIWIRI: AHEBERI 5: 7-9
UTHENGA WABWINO: YOHANE 12: 20-33

ONANI, NDIKUPANGA PANGANO LATSOPANO

Mucowerenga cathu choyamba tsiku la lero, mprofeti Yeremiya akudzisonyeza kukhala munthu wosakondwa ndiponso wosagwirizana ndi makhalidwe a ana a Israele. Mprofetiyu atumidwa kukalalika mau a Mulungu ku anthu amene alephera kusunga pangano. Imeneyi sinchito ya pafupi kwa munthu aliyense. Nthawi zambiri Yeremiya apezeka akulalika uthenga wa cionongeko mwa cisoni ndithu. Monga momwe zimakhalira nthawi zambiri; anthu alephera kusiyanitsa pakati pa uthenga (wacisoni) ndi mthenga (Yeremiya) ndipo acita naye molinganiza ndi malingaliro awo; kotero kuti nthawi zambiri Yeremiya akanidwa, anyozedwa ndi kuponyedwa m'ndende.

Komabe, ngakhale zinthu zioneke zacisoni motero, Yeremiya ayetsetsa kusonkhanitsa ciyambi catsopano kucokera m'mabwinja. Ngakhale kuti Yeremiya sanali kuona ubwino uli wonse, anagonjera m'maganizo kuti Yahweh anali kucita cinthu cina catsopano. Uyu ndi umboni weni-weni wonena kuti Yahweh salephera konse kapena kutaya mtima. Ngakhale kuti pangano likhalila mbali ziwiri, kusakhulupirika kwa mbali imodzi sikusonyeza kusakhulupirika kwa mbali ina ija. Popeza kuti anthu alephera kusunga pangano loyamba lija, Mulungu ndi wokonzeka kucita nao pangano lina latsopnali.

Cimeneci ndi cifukwa cokwana codzetsera cikondwerero ndi cikhulupiriro ca ubwino m'zonse. Tonse tidziwa bwino momwe talepherera kusunga mapangano athu osiyana-siyana: malonjezano a ubatizo wathu, ukwati wathu, unsembe wathu, mbindikiro zina kapenanso moyo wina uliwonse wa m'chipani; ngakhalenso mu malonjezano a malonda ena! Sitifuna konse aprofeti otiuza za kulephera kwathu popeza kuti kwatilemetsa kale. Zomwe tifuna kuzimva ndi izi: "**Onani ndikupanga pangano latsopano**." M'njira ina, titha kunena kuti Mulungu wayamba kale kucita cinthu cina catsopano ndipo ndi nchito yathu kuti tikhale amodzi mukufuna kwabwinoku. Zoonadi mulungu ali kutiitana kuti tilowe mu pangano latsopnali ndi kuyamba bwino moyo wathu. Paja mwambi unena kuti *"pomwe Mulungu wakonzera pwando, sipaoneka utsi."* Tsono comwe cifunika kwa ife akhristu ndi kubvomera kuitanaku kwa Mulungu mokhulupirika.

Tonse tibvomereza kuti dziko lathu la Zambia liri m'njira losanda-sanda malamulo a dziko(Constitution Review) ndi colinga coti tikhale nao malamulo atsopano omwe adzalimbana ndi *"muyeso wa nthawi."* Tonse tikhulupirira kuti tizayendetsa masankho a dziko lathu caka cino potsata malamulo atsopanowa, ndipo kuti masankho amenewa adzakhala angwiro ndi obvomerezedwa pamaso pa anthu onse. Tonse tikhulupirira kuti ndife ounguzidwa pa za ufulu, nchito ndi mphamvu zathu ngati mbadwo(citizens) za dziko la Zambia. Tasiyana ndi m'mene tinaliri zaka zisanu zapitazi. Motero, ndife okonzeka kufunsa kapena kuzuzula atsogoleri athu maninga ndi m'mene alamulira dziko lathu. Ici ndi cinthu catsopano m'cikonzekelo, ndipo ngati simulinafe pamodzi pa njira, ndiko kuti muli m'njira!

Koma pamenepa pali cinsisi. Ubwino watsopanowu kuti ucitike ndi kupselezeraka, pafunika kukhoza mayeso ena ace. Ndipo m'yesowu taumva mu Uthenga Wabwino m'mau akuti: *"mbewu ya tirigu ikapanda kugwa munthaka ndi kufa, imakhala yokha, koma ikafa, imabereka zipatso zambiri."* Ubwino watsopanowu umene Mulungu akubweretsa pakati pathu ungathe kuoneka maso ngati ife tomwe tidzipereka ku imfa. Zoonadi, tiyenera kufa kuzinthu zambiri zokhalira ife tokha pacathu chifukwa ca anthu onse. Kodi nkutheka bwanji kuti zipani zandale zosiyana-siyana zikhale pamodzi ndikugwira nchito pamodzi mu ubwino wa onse m'dziko lathu ngati palibe kuzipereka ndi kuzimana? Kodi

JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION
"Promoting Faith and Justice"
P.O. Box 37774 10101 Lusaka, Zambia
E mail: jctr@jesuits.org.zm

tingayembekeze bwanji kukhala ndi malamulo atsopano popanda wina aliyense kaya magulu a anthu kuzipereka ndi kuzimana, n'colinga cofuna kubereka moyo wolimba wa dziko lathu?

Zolinga zonsezi zitha kukwanilitsidwa ngati taphunzira kuika ubwino wa dziko lathu patsogolo. Madziko atatu a machalitchi muno mwathu mu Zambia- *Evangelical fellowship of Zambia (E.F.Z), Zambia Episcopal Conference (ZEC) ndi Council of Churches (CCZ)*- mu kalata yawo kwa akhristu onse pa nthawi yoyembekezera matsankho a caka ca 1991, ananena kuti: *cinthu cofunika kweni-kweni mu matsankho ciyenera kukhala cilako-lako ca ubwino wa onse mziko. Ngakhale kuti papezeke kusiyana kwa zipani, ndife anthu a dziko limodzi, abale ndi alongo m'coliga copititsa dziko lathu patsogolo.*

Pa Sabata lino la cisanu mu nyengo ino ya Lenti, nyengo yodzadza ndi caulere, tipemphere ndi kuthokoza Mulungu pa zizindikiro zambiri zomwe zipezeka m'zimbumba zathu, zimene zikusonyeza ndithu kuti cinthu cina catsopano cili kucitika. Pemphero lathu likhale lakuti matsankho a caka cino akhale gwero lathu lotipititsa patsogolo m'njira yabwinoyi ndikutibweretsa pamodzi pakukometsa dziko lathu lino la Zambia. Tipempherenso kuti mu nyengo ino ya Lenti, tonse tipeze nthawi yokhala pansi pafupi ndi mtanda wa Ambuye Yesu ndikuphunzirako nzeru zozama pobvomera kuti moyo weni-weni umabwera ngati tabvomera kupacikidwa ndi kufa. Mulungu akutiuza kuti: **"Onani, ndikupanga pangano latsopano."**

Kusinkha-sinkha mafunso ndi kugawana mzimbumba

- Kodi ndasunga mapangano anga a ubatizo, ukwati, unsembe kapena moyo wina uliwonse wa m'chipani?
- Kodi ndili okonzeka kucita pangano lina latsopano ndi Mulungu?
- Kodi tili okonzeka kugwira ntchito pamodzi ndi mamembala ena a zipani zandale zosiyana-siyana n'colinga cofuna kubwertsa citukuko m'mambumba mwathu?

Sewero

Pakhale banja la awiri. Iwowa akhala pamodzi kwa kanthawi ndithu. Ndipo wina aswanya pangano posakhulupirika. M'zace wokhumudwa akhululuka ndipo ayanjana. Motereo, ayamba moyo watsopano ndipo banja lonse lisangalala nao pamodzi chifukwa ca cimwemwe comwe cabwereranso.

Mapephero a mbumba

- Ambuye, tipemphera mothokoza ndithu pa zizindikiro zambiri zomwe zipezeka m'zimbumba zathu zimene zikusonyeza kuti cinthu cina catsopano cikucitika mu moyo wathu…**Ambuye mutimvere! Tikupemphani mutimvomereze!**
- Ambuye, tikupempha m'caka cino ca matsankho kuti tiyendere limodzi ndi kukhala amodzi pakubweretsa ubwino wa dziko lathu la Zambia…**Ambuye mutimvere! Tikupephani mutimvomereze!**
- Ambuye, tikupempha kuti pomwe tikuyandikira cikondwerero ca pasaka, tipeze nthawi yokhala pansi pafupi ndi mtanda wanu ndikuphunzirako nzeru zoti moyo weni-weni umabwera ngati tabvomera kuzimana, kupacikidwa ndi kufa pamtanda… **Ambuye mutimvere! Tikupephani mutimvomereze!**

JESUIT CENTRE FOR THEOLOGICAL REFLECTION
"Promoting Faith and Justice"
P.O. Box 37774 10101 Lusaka, Zambia
E mail: jctr@jesuits.org.zm